

CHIKALATA CHA UTHENGA WA KAFUKUFUKU CHA KHOLO WOYANG'ANIRA – ANA A ZAKA 1 MPAKA 5 - AKUDERA

DZINA LA KAFUKUFUKU: **TIMASAMALA** (Kupeza amene anapumako tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu - Tuberculosis Immunoreactivity Surveillance in Malawi)

MALO A KAFUKUFUKU : **Kudera**

WAMKULU WOCHITITSA KAFUKUFUKU: Dr Hannah Rickman

MAU OYAMBA

Mulikuitanidwa kuti mwana wanu atenge nawo mballi mu kafukufuku wokhudzana ndi matenda a chifuwa chachikulu cha TB mwa ana ang'onoang'ono, ndipo ngati simukufuna kutenga nawo mbali mukafukufukuyu, sidzikhudza chisamaliro cha ku chipatala chomwe mu njira ina iliyonse. Tiwerenga limodzi uthenga umeneu komanso kuyankha mafunso ena alionse amene mukhoza kukhala nawo.

Kafukufukuyu akuchitika mothandizidwa ndi ndalama zochokera ku bungwe la Wellcome Trust ndipo akuchitika ndi bungwe la Malawi Liverpool Wellcome Programme mogwirizana ndi sukulu ya ukachenjede ya London School of Hygiene & Tropical Medicine komanso ndi a ofesi yoona za umoyo ya Blantyre District Health Office. Kafukufukuyu achitika kwa zaka ziwiri. Anthu okwana 4,500 akuyembekezereka kulowa mu kafukufuku ameneyu. Kafukufukuyu wavomerezeka ndi makomiti oona za ufulu wa kafukufuku a sukulu ya ukachenjede a Kamuzu University of Health Sciences College of Medicine Research Ethics Committee, komanso ndi a London School of Hygiene and Tropical Medicine Research Ethics Committee.

Chikalata cha uthenga cha wotenga mbalichi chikuthandizani kupanga chisankho ngati mukufuna mwana wanu kutenga nawo mbali. Chikalatachi chikufotokoza chifukwa chimene tikuchitira kafukufukuyu, kuti atenge nawo mbali kwa mwana wanu kukhala kotani, phindu ndi ziopsyezo zimene zikhoza kukhalapo, komanso zimene zitadzachitike kafukufukuyu akatha.

Simukuyenera kupanga chisankho tsiku la lero choti mwina mukhoza kutenga nawo mbali mu kafukufukuyu. Musanapange chisankho mwina mukhoza kufuna kulankhula ndi anthu ena zokhudzana ndi kafukufukuyu, monga anzanu, kapena wopereka chisamaliro cha za umoyo. Khalani omasuka kutero. Ngati inu kapena anthu a mubanja mwanu komanso anzanu akufuna uthenga woonjezera, chonde musakaike kulumikizana naye.




**Malawi-Liverpool-Wellcome Trust
Clinical Research Programme**

P.O Box 30096, Chichiri, Blantyre 3, Malawi.

Tel. +265 1 876444 Fax +265 1 875774

Mukavomera kuti mwana wanu atenge nawo mbali mu kafukufukuyu, mupemphedwa kuti musainire chikalata cha chilolezochi chimene chili kumapeto kwa chikalata ichi. Mupatsidwa chikalata cha uthenga cha wotenga nawo mbali ndi chikalata cha chilolezo.

Chonde onetsetsani kuti mwawerenga ndi kumvetsa masamba onse a chikalatachi.




KODI CHOLINGA CHA KAFUKUFUKUYU NDI CHANI ?

Matenda a chifuwa chachikulu(TB) ndi vuto lalikulu kwambiri m'Malawi muno. Tikufuna tione ngati kuyeza kupezeka kwa tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu mwa ana kumakiliniki komanso kumadera kwawo kungathandize kupeza ana amene akhudzidwa ndi matenda a chifuwa cha chikulu , komanso kupeza malo kumene kuli chiopsyeyo chachikulu cha matenda a chifuwa chachikulu mu mzinda wa Blantyre, ndipo madera amenewa akhoza kupindula pounikidwa mwapadera ndi kulandira chithandizo.

KODI KUTENGA NAWO MBALI KWA MWANA WANGA KUKHALA KOTANI ?

Tikupempha chilolezo kuti Mwana wanu atenge nawo mbali chifukwa ali ndi zaka pakati pa chaka chimodzi kulekeza zisanu (1-5) ndipo amakhala ku Blantyre kumene tikuchitako kafukufuku. Mukalola kuti mwana wanu atenge nawo mbali, titenga magazi kuti tiyeze munjira yotchedwa 'IGRA' imene imayeza ngati mwana anapumako mpweya wokhala ndi tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu pa moyo wake.

1. Anamwino akufunsani mafunso okhudzana ndi umoyo wa mwana wanu komanso pakhomu panu, komanso komwe mumakhala. Mwa anthu ena ochepa, tidzakuyenderani pakhomu panu,	  20 min
2. Anamwino amutenga mwana wanu magazi okayeza okwana 5mL (pafupifupi supuni imozi ya tiyi). Magazi amenewa akayezedwa kuti tione ngati mwana wanu anapumako mpweya wokhala ndi tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu. Mtsogolo muno magazi otsala akhoza kukayezedwa zizindikiro za chitetezo cha mthupi ku matenda a chifuwa chachikulu komanso matenda ena.	  5 min
3. Zotsatira zikasonyeza kuti mwana wanu sanapumeko tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu tidzakutumizirani SMS mu sabata ziwiri KAPENA mukhoza kuimba foni ku 0992090160. KAPENA kupita ku chipatala cha Bangwe / Limbe / Ndirande kuti mukatenge zotsatira pakadutsa sabata ziwiri. Zotsatira zikasonyeza kuti mwana wanu anapumako tizirombo toyambitsa	 

matenda a chifuwa chachikulu, tidzakuyimbirani foni ndipo tikhoza kudzakuyenderani, kuti tikonze dongosolo lomuunika mwanayo mwapadera ndi kupereka chithandizo cha mankhwala	
---	--

Kuyeza magazi kudzakahala Kotani?

Kuyeza magazi kudzakachitika ku malo oyezerako chifuwa chachikulu pounika zizindikiro zoonetsa ngati munthu anapumako mpweya wokhala ndi tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu. Kuonjezera apo, kuyeza kukhoza kuchitika pa magazi poonamo matenda ena, komanso zoonetsera chitetezo cha mthupi chomenyana ndi matenda a chifuwa chachikulu. Zotsatira zoonjezerazi zidzaperekedwa kwa inu ngati zingathandize kupititsa thanzi la mwana wanu patsogolo, kapena ngati inu mudzafunse. Zonse zotengadwa kukayeza zidasungidwa kwa zaka zisanu kafukufukuyu akatha ndipo kenaka zidzaonongedwa.

Nanga ngati zoyeza zatuluka kuti zili ndi matenda?

Mu maiko monga Malawi, sizachilendo kuti ana apezeke kuti anapumako tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu. Izi sizikutanthauza kuti mwanayu ali ndi matenda a chifuwa chachikulu pakadali pano kapena kuti akhoza kupatsira anthu ena. Ngati mwayo ali ndi zindikiro za matenda a chifuwa chachikulu pano, tidzakupatsani chikalata choti mupite nacho ku chipatala cha ana ku Queen Elizabeth Central Hospital. Ana ena amene zoyeza zawo zawnetsa kuti anapumako mpweya wokhala ndi tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu akhoza kudzadzala matendawa mtsogolo, choncho ngakhale ali bwino, tidzawatumizabe ku kiliniki ya chifuwa chachikulu ku chipatala cha kudera kwanu kumene angapatsidwe mankhwala ochepetsa chiopsezo chodzadzala matenda a chifuwa chachikulu cha TB mtsogolo. Chithandizo chimenechi ndi chaulele. Tidzafunanso kuti anthu onse okhala m'nyumba momwe mumakhala mwana uyu kuti aunikidwe ngati ali ndi chifuwa chachikulu ndipo tidzawapatsa timabitolo totengeramo makhololo.

Mbiri yokhudzana ndi mwana

Tikufunsani mafunso okhudzana ndi umoyo wa mwana wanu komanso wa anthu a pakhomu panu, amene akhoza kukhala mafunso ovutirapo kuyankha. Mayankho onse adzasungidwa mwa chinsinsi.

Maakafukufuku ena

Tikhozanso kulumikizana nanu kuti tikufunseni zokhudzana ndi zimene mwakumana nazo pa kuyeza magazi komanso pokhala mu kafukufuku. Pamenepo, tidzakuitanani kukafukufuku oonjezera okufunsani mafunso, pamene mudzathokozedwa chifukwa cha nthawi yanu. Izi zidasungidwa mwachinsinsi. Mukhoza kutenga nawo mbali mu akafukufuku ofunsidwa kupereka maganizo anu pakufukuyi ngakhale musakufuna kutenga nawo mbali mu kafukufuku wamkulu.

KODI PHINDU NDI ZIOSYEZO MU KAFUKUFUKUYU NDI ZOTANI?

Phindu lotenga nawo mbali mu kafukufukuyu kwa mwana wanu ndi loti tikhoza kupeza matenda a chifuwa chachikulu mwamsanga, zimene zikhoza kuthaniza kuti mwana wanu asadwale matenda a chifuwa chachikulu ngati atalandira mankhwala. Tikhozanso kupeza maatenda a chifuwa chachikulu mwa anthu a mubanja la mwanayu. Kuonjezera apo, kutenga nawo mbali kwa mwana wanu kukhoza kuthandiza poonjezera nzeru za sayansi zimene zikhoza kuthandizira anthu mu dziko la Malawi komanso padziko lonse la pansi kupeza njira zofufuzira komanso zotetezera kutenga tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu.

Chiopsezo chimodzi potenga nawo mbali mukafukufukuyu ndi choti kutenga magazi kukhoza kukhala kosowetsa mtendere kwa mwana. Tidzatenga magazi okwana supuni ya tiyi imodzi yokha basi, ndipo zimenezi sizingabweretse vuto lina lililonse kwa mwana wanu. Chiopsyezo china ndi chakuti nthawi zina zotsatira za kuyeza magazi za mwana wanu zikhoza kuonetsa ngati anapumako tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu koma asanapumeko. Izi zikutanthauza kuti akhoza kulandira mankhwala otetezera kuti asadwale chifuwa chachikulu pamene iye asali pachiopsezo chachikulu. Mankhwala nthawi zina amatha kupangitsa kuti munthu aone zizindikiro zosowetsa mtendere.

NDI NDANI AMENE AAKULIPIRA KUTENGA NAWO MBALI MU KAFUKUFUKUYU?

Agulu la kafukufuku sakuyenera kukufunsani zokomera iwo (Ndalama, kukugwirani thupi kapena kugona nanu) potengerapo mwayi chifukwa mwatenga nawo mbali mu kafukufukuyu. Mudzathokozedwa ndi Ndalama zokwana 3000 Kwacha chifukwa cha nthawi yomwe mwataya potenga nawo mbali mu kafukufukuyu. Kwa anthu ochepa, tidzakuyenderani kunyumba kwanu kuti tidzaone ngati tinatenga ma adilesi olondola; ngati titadzapange zimenezi tidzakuuzani tsikulo lisanafike ndipo tidzakuthokozani ndi 1000 Kwacha. Ngati zotsatira zamwana zaonetsa kuti anapumako tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu, ndipo mwana akufunika zoyeza zoonjezera ku kiliniki, tidzakupatsani ndalama yokuthandizirani mayendedwe. Kuonjezera apo, ngati zoyeza zatuluka kuti mwana anapumako tizirombo toyambitsa matenda a chifuwa chachikulu, tidzakupatsani mabotolo okaikamo makhololo a anthu okhala m'nyumba imodzi ndi mwanayo kuti apititse kuchipatala, ndipo akapereka mabotolo adzalandira 2500 Kwacha chifukwa cha nthawi yomwe mwataya ndi ndalama yomwe mwagwiritsa ntchito pa mayendedwe. Kwa amene akutenga nawo mbali mu kafukufuku wokambirana wopereka maganizo awo pakufukuyu adzathokozedwa ndi ndalama ina yoonjezera yokwana 5000 Kwacha chifukwa cha nthawi yawo.

KODI UFULU WANGA NDI WOTANI ?

Kutenga nawo mbali kwanu mu kafukufukuyu ndi kosakakamizidwa. Muli ndi ufulu woletsa mwana wanu kutenga nawo mbali, kapena kusiya kutenga nawo mbali mu kafukufuku nthawi

ina iliyonse, opanda kukumana ndi zovuta zili zonse. Muli ndi ufulu kuona uthenga wokhudzana ndi inu ndi umene watoleredwa ngati mbali ya kafukufuku komanso kuuzidwa zokhudzana ndi uthenga uliwonse watsopano wobwera m'kafukufuku. Uthenga wotolera wokhudzana ndi inu ungathe kuonedwa ndi a gulu la kafukufuku, kuphatikizapo wamkulu wa komiti yoona za ufulu wa anthu mu kafukufuku ya Ethics Committee ndi oyang'anira malamulo a kayendedwe ka kafukufuku, komanso oyang'anira kayendedwe ka kafukufuku.

CHITETEZO

A gulu la kafukufuku ndi otolera uthenga mu kafukufuku akuyembekezereka kukhala ndi khalidwe loyenerera komanso kukhala ndi udindo nthawi ina iliyonse ndi kutsatira malamulo a anthu ogwira ntchito ku bungwe la MLW. Izi zikutanthauza kuti sakuyenera kukupemphani ndalama, thupi lanu kapena kugona nanu potengerapo mwayi chifukwa mwatenga nawo mbali mu kafukufuku uyu. Ngati mungakumanane ndi nkhanza, kupwetekedwa mtima kulikonse kapena kusasamalidwa ndi wa mu gulu la kafukufuku, mukhoza kulumikizana ndi oona za chitetezo a ku bungwe la MLW poimba pa 0881 537 472. Mukhoza kuimba nambala imeneyi nthawi ina iliyonse. Komanso, mukhoza kupeza chithandizo kuchokera ku One Stop Centre ku chipatala cha Queen Elizabeth Hospital(0999 77 292(uphungu) kapena kulemba imelo pa onestopcentre.bt@gmail.com).

CHITACHITIKE NDI CHANI KAFUKUFUKUYU AKATHA?

Zopezeka mu kafukufukuyuyu zidzaperekedwa kwa anthu zikavomerezedwa ndi onse oyenerera ogwira nawo ntchito. Zotolera zokhudzana ndi inu zidasungidwa kwa zaka zosapitirira zisanu kafukufukuyuyu akatha. Zotolera zomwe sizikukhudzana ndi inu zikhoza kusungidwa kuti zidzaunikidwe moonjezera pa kafukufuku wina wofanana ndi uyu. Mukavomera, zotolera zopanda dzina (zimene sizingakuzindikiritseni inu kapena mwana wanu) zikhoza kugawidwa kwa ochita kafukufuku ena padziko lapansi kuti achite kafukufuku oonjezera.

KODI NDILUMIKIZANE NDI NDANI KUTI NDIMVE ZAMBIRI ?


Ngati muli ndi mafunso alionse, nkhwana kapena madandaulo okhudzana ndi kafukufukuyuyu pa gawo lililonse la kafukufukuyuyu, mukhoza kulumikizana ndi :

Frank Chikapa, Senior Fieldworker, Public Health Group
0999981674 | fchikapa@mlw.mw

Komanso, mukhoza kulumikizana ndi wapampando wa komiti yoona za ufulu wa anthu mukafukufuku a College of Medicine Research Ethics Committee amene amayang'anira kafukufuku yense, poimba foni pa 0888 118 893, kapena kulemba email ku

TIMASAMALA - Chichewa PIL/consent (children 1-5, community)

1 February 2023 v5.0






**Malawi-Liverpool-Wellcome Trust
Clinical Research Programme**

P.O Box 30096, Chichiri, Blantyre 3, Malawi.

Tel. +265 1 876444 Fax +265 1 875774

comrec@medcol.mw kapena kulemba kalata pa adilesi iyi COMREC Secretariat, College of Medicine, P/bag 360, Blantyre 3. Kafukufukuyu waunikidwanso ndi kuvomerezedwa ndi a komiti yoona ufulu wa anthu mukafukufuku a College of Medicine Research and Ethics Committee (COMREC) ku Blantyre. Komiti imeneyi imaonetsetsa kuti anthu otenga nawo mbali mukafukufuku ndi otetezedwa.



CHIKALATA CHA CHILOLEZO CHA KHOLO/OYANG'ANIRA ANA WOTENGA NAWO
MBALI A ZAKA 1 MPAKA 5 - AKUDERA

Dzina la wotenga nawo mbali _____

Nambala ya chidziwitso yaw otenga nawo mbali _____

[Dzina la wotenga nawo mbali ndi nambala ya chidziwitso zilembedwe woyang'anira
wodwala akasainira chikalata cha chilolezo]

TIMASAMALA

*Chonde yankhani mafunso otsatirawa poika zilembo zoyamba za maina kapena chidindo
chachala ku yankho loyenerera*

Funso	Initial/ chidindo oyang'anira satha kuwerenga/kulemba kapena cha omwe
Ndawerenga kapena andiwerengera chikalata cha uthenga cha wotenga nawo mbali cha kafukufukuyu ndipo andifotokozera tsatanetsatane wa kafukufukuyu	
Mafunso anga okhudzana ndi kafukufukuyu ayankhidwa mokwanira ndipo ndikumvetsa kuti ndikhoza kufunsa mafunso oonjezera nthawi ina liyonse.	
Ndikumvetsa kuti ndine omasuka kuchotsa chilolezo cha mwana wanga chotenga nawo mbali mu kafukufukuyu nthawi ina iliyonse opanda kupereka chifukwa chilichonse, opanda kusokoneza chhisamaliro choyenerera cha kuchipatala.	
Ndikuvomera kupereka uthenga kwa ochititsa kafukufuku pansu pa malamulo osunga chinsinsi amene alembedwa mu chikalata cha wotenga nawo mbali.	
Ndikuvomera kuti a gulu la kafukufuku alumikizane nane pa chifukwa cha zotsatira za zoyeza za mwana wanga. Ngati zotsatira zili ndi chifuwa chachikulu ndipo sanagalumikizane nane, ndikuvomera kuti iwo abwere kunyumba kwanga kuti aonetsetse kuti ndalandira zotsatira..	
Ndikuvomera kuti ogwira ntchito ya kafukufuku athe kuona zolemba za chipatala zokhudzana ndi mwana wanga zogwirizana ndi kafukufuku uyu	
Ndikuvomera kuti uthenga wotolera wokhudzana ndi mwana wanga wopanda dzina wokhudzana ndi ine ugawidwe kwa wochititsa kafukufuku ena padziko la pansu (kukhala ndi mwayi oona zotolera) kwa nthawi yaitali ndipo pa chifukwa chilichonse, komanso kutenga uthenga womwe aphunzirapo kuuika mu zolemba za sayansi.	

Ndikuvomera kuti mwana wanga atenge nawo mbali mu kafukufukuyu pansi pa malamulo amene alembedwa mu chikalata cha uthenga cha wotenga nawo mbali.	
Zosankha	
Ndikuvomereza kuti a gulu la kafukufukuyu adzabwe kunyumba kwanga ndi cholinga chotsimikiza malo a dilesi yanga(izi zidzachitika kwa anthu ochepa otenga nawo mbali mosankha opanda dongosolo) consent for research team	
Ndikupereka chilolezo agulu la kafukufu adzalumikizansenso nane kuti nditenge nawo mbali mu kafukufuku wofunsa mafunso oonjezera amene sanatchulidwe mu chikalata cha uthenga cha wotenga nawo mbali koma wofanana ndi ndi kafukufuku uyuyu..	
Ndikupereka chilolezo kuti magari anga okayeza adzagwiritsidwe ntchito pa kafukufuku oonjezera wokambirana pofunsa mafunso amene sanatchulidwe mu chikalata cha uthenga cha wotenga wotenga nawo mbali koma ndi wogwirizana ndi funso la kafukufuku uyu.	

CHIKALATA CHA CHILOLEZO CHA KHOLO/OYANG'ANILA ANA A ZAKA 1 MPAKA 5 - AKUDERA

Dzina la wotenga nawo mbali _____

Nambala ya chidziwitso yaw otenga nawo mbali _____

[Dzina la wotenga nawo mbali ndi nambala ya chidziwitso zilembedwe woyang'anira
wodwala akasainira chikalata cha chilolezo]

TIMASAMALA

Dzina la wotenga nawo mbali :

Dzina la mwana wotenga nawo mbali		
Dzina la oyang'anila mwana otenga mbali mu kafukufuku	Tsiku	Siginitchala /chidindo cha chala
Dzina la mboni yosatengela mbali	Tsiku	siginitchala
Dzina la wamugulu la kafukufuku amene akutenga chilolezo	Tsiku	Siginitchala

Ubale ndi mboni yosatengera mbali: _____